Charity

Chikondi Chapamwamba Kwambiri

Zinthu zanu zonse zichitike ndi chikondi.

1 Akorinto 16:14

Ngakhale ndilankhula malilime a anthu ndi a angelo, ndipo ndiribe chikondi, ndikhala ngati mkuwa wolira, kapena nguli yolira.

Ndipo ndingakhale ndiri ndi mphatso ya kunenera, ndipo ndingamvetse zinsinsi zonse, ndi chidziwitso chonse; ndipo ndingakhale ndiri nacho chikhulupiriro chonse, kotero kuti ndikasendeza mapiri, koma ndiribe chikondi, sindili kanthu.

Ndipo ndingakhale ndipereka chuma changa chonse kudyetsa osauka, ndipo ndingakhale ndipereka thupi langa alitenthe m'moto, koma ndiribe chikondi, sindipindula kanthu.

Chikondi chikhala chilezere, chiri chokoma mtima; chikondi sichidukidwa; chikondi sichidzikuza, sichidzikuza, sichichita zosayenera, sichitsata za mwini yekha, sichipsa mtima msanga, sichilingirira zoipa; Sichikondwera ndi kusayeruzika, koma chikondwera ndi choonadi; Chikwirira zinthu zonse, chikhulupirira zinthu zonse, chiyembekeza zinthu zonse, chipirira zinthu zonse.

Chikondi sichitha nthawi zonse: koma ngati pali maulosi, adzalephera; kapena malilime, adzaleka; ngakhale kudziwa, kudzasowa.

Pakuti tidziwa mderamdera, ndipo timanenera mderamdera. Koma pamene chimene chiri changwiro chafika, pamenepo chimene chiri chamderamdera chidzachotsedwa. Pamene ndinali mwana, ndinalankhula ngati mwana, ndinaganiza ngati mwana, ndinaganiza ngati mwana; Pakuti tsopano tipenya ndi kalilole ngati mdima; koma pamenepo maso ndi maso: tsopano ndidziwa mderamdera; koma pamenepo ndidzazindikira, monganso ndidziwika.

Ndipo tsopano zitsala chikhulupiriro, chiyembekezo, chikondi, zitatu izi; koma chachikulu cha izi ndicho chikondi.
1 Akorinto 13

Dikirani, chirimikani m’chikhulupiriro, khalani amuna, khalani olimba. Zinthu zanu zonse zichitike ndi chikondi. **1 Akorinto 16:13-14**

Chifukwa chake bvalani, monga osankhika a Mulungu, oyera mtima ndi okondedwa, mtima wachifundo, kukoma mtima, kudzichepetsa, chifatso, kuleza mtima; kulolerana wina ndi mzake, ndi kukhululukirana eni okha, ngati wina ali nacho chifukwa pa mnzake; Ndipo koposa zonsezi valani chikondi, ndicho chomangira cha ungwiro. Ndipo mtendere wa Mulungu uchite ufumu m’mitima mwanu, kumene munaitanidwanso m’thupi limodzi; ndipo khalani othokoza. **Akolose 3:12-15**

Chisomo kwa inu, ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate wathu ndi Ambuye Yesu Khristu. Tiyenera kuyamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu, abale, monga kuyenera; kotero kuti ife tokha tidzitamandira mwa inu m’Mipingo ya Mulungu, chifukwa cha chipiriro chanu, ndi chikhulupiriro chanu, m’mazunzo anu onse ndi masautso mupirira; **2 Atesalonika 1:2-4**

Koma chitsiriziro cha lamulo ndicho chikondi chochokera mu mtima woyera, ndi chikumbumtima chabwino, ndi chikhulupiriro chosanyenga: **1 Timoteo 1:5**

Pakuti chifukwa cha ichi tigwira ntchito ndi kutonzedwa, popeza tikhulupirira Mulungu wamoyo, amene ali Mpulumutsi wa anthu onse, makamaka wa iwo akukhulupirira. Zinthu izi lamulira, nuphunzitse. Munthu asapeputse ubwana wako; koma ukhale chitsanzo cha iwo akukhulupirira, m’mawu, m’mayendedwe, m’chikondi, m’chikhulupiriro, m’kuyera mtima. Kufikira ndidza Ine, samalira kuŵerenga, kudandaulira, ndi chiphunzitso.
1 Timoteo 4:10-13

Koma m’nyumba yaikulu simuli zotengera za golidi ndi zasiliva zokha, komanso za mtengo ndi dothi; ndi zina za ulemu, ndi zina zopanda ulemu. Ngati tsono munthu adziyeretsa yekha pa izi, adzakhala chotengera cha ulemu, chopatulika, choyenera kuchita nacho Mbuye, chokonzera ntchito yonse yabwino. Thawanso zilakolako zaunyamata, koma tsata chilungamo, chikhulupiriro, chikondi, mtendere, pamodzi ndi iwo akuitana pa Ambuye ndi mtima woyera. Koma mafunso opusa ndi opanda nzeru upewe, podziwa kuti amabala ndewu.
2 Timoteyo 2:20-23

Koma citsiriziro ca zinthu zonse ciri pafupi; Ndipo koposa zonse khalani nacho chikondano chenicheni mwa inu nokha: pakuti chikondi chidzakwirira unyinji wa machimo. Mucherezane wina ndi mnzace, osadandaula. **1 Petulo 4:7-9**

Ndipo mwa ichi, ndi changu chonse, kuwonjezera pa chikhulupiriro chanu ukoma; ndi pa ukoma chidziwitso; ndi pa chidziwitso chodziletsa; ndi pa chodziletsa chipiliro; ndi pachipiriro chipembedzo; Ndi pa chipembedzo chikondi cha pa abale; ndi pa chikondi cha pa abale chikondi. Pakuti ngati zinthu izi zili mwa inu, ndipo zikachuluka, zidzakupangani kuti musakhale aulesi kapena opanda zipatso pa chidziwitso cha Ambuye wathu Yesu Khristu. **2 Petulo 1:5-8**